



09400521

**EXAMINATIONS COUNCIL OF ZAMBIA****Examination for School Certificate Ordinary Level****Cinyanja****3156/2****Pepala Laciwiri****Monday****14 NOVEMBER 2022****Zina Zofunikira:****Buku la Mayankho****Nthawi: Maola Awiri****Makisi: 100****Malangizo Kwa Olemba Mayeso**

- 1 Lemba **nambala yamalo** komwe ulemba mayeso ndiponso **nambala yako iwe amene ulemba mayeso**. Ulemba izi m'malo omwe apatsidwa mukabuku kamayankho.
- 2 Pepala la mayeso iri liri ndi zigawo zinai **A, B, C** ndi **D**.
- 3 Ukakamizidwa kuyankha mafunso onse opezeka pacigawo ciriconse ca pepala lino.
- 4 Lemba mayankho ako m'kabuku ka mayankho komwe kapatsidwa.
- 5 Ngati wagwiritsira nchito mopitirira kabuku kamodzi, umange pamodzi mwatsatane-tsatane timabuku tonse timene wagwiritsa nchito.
- 6 Uziwerenga mobwereza-bwereza ndi kumvetsetsa malangizo omwe alembedwa pamwamba pafunso liri lonse.

Zina Zolangiza Olemba

- 1 Nambala ya mamaliki yaikidwa mu mfungato [], kumatsiriziro kapena kumbali kwa funso liri lonse, mwatsatane-tsane.
- 2 Malamya yam'manja **siyaloledwa** m'cipinda colemba mayeso.

A CIGAWO COYAMBA – CINENENDWE: [MAKISI: 30]
Ukakamizidwa kuyankha mafunso onse asanu amene ali m'cigawo cino.

- 1 Pereka cimake ca m'neni ullonse umene wapatsidwa munsimu. [1]
 - (a) Phika [1]
 - (b) Langa [1]
 - (c) Lima [1]
 - (d) Lemba [1]
 - (e) Thamanga [1]
 - (f) Umba [1]
- 2 (a) Kopdi afotokozi ndi mau otani? [2]
 - (b) Panga ziganizo pogwiritsa nchito matsinde awa: [2]
 - (i) -yera [2]
 - (ii) -mbiri [2]
- 3 Pereka dzina lopezeka m'magulu opatsidwa awa m'cimodzi ndi kuculukitsidwa kwake.

Citsanzo: 1. Mu	2. A	
Dzina m'cimodzi: Munthu	kuculukitsa: Anthu	

 - (a) 3. Mu 4. Mi [2]

Dzina m'cimodzi: _____	m'kuculukitsa: _____
------------------------	----------------------
 - (b) 7. Ci 8. Zi [2]

Dzina m'cimodzi: _____	m'kuculukitsa: _____
------------------------	----------------------
 - (c) 12. Ka 13. Ti [2]

Dzina m'cimodzi: _____	m'kuculukitsa: _____
------------------------	----------------------
- 4 Panga aneni kucokera ku maina awa:
 - (a) bvuto [1]
 - (b) phindu [1]
 - (c) mpulumutsi [1]
 - (d) Ndakatulo [1]
 - (e) mthandizi [1]
 - (f) ciweruzo [1]
- 5 Panga ziganizo zoyenera ndi zidunswa za mau izi kusonyeza nthawi
 - (a) -da- [2]
 - (b) -nali [2]
 - (c) -ma- [2]

B CIGAWO CACIWIRI – TEMBENUZO: [MAKISI: 20]

Ukakanizidwa Kuyankha funso lotsatirali m'Cinyanja comveka bwino ndiponso coyenera. Tsopano tembenuza nkhani imene iri munsimu.

Shame and Guilt

Shame causes one to feel guilty but there is a difference between the two. You do not need anyone to make you feel guilty. Every person that feels guilty judges himself.

Shame is however different. The feeling of shame requires another person to make you realise. They either have to mock or disapprove your action to make you realise your wrong. If no one except yourself knows your wrong, there will be no feeling of shame, but the feeling of guilt for the wrong committed remains.

Shame, like guilt, is like everything else we live with; it is something we live with for a long time. They say: "Soap cannot wash away your shame". And a renowned writer of past years added: "Live in your shame, but don't die with your shame". Even when we do wrong, to avoid dying with shame, apology is helpful, but shame is not.

C CIGAWO CACITATU – MVETSO [MAKISI: 30]

Werenga nkhani iri munsimu ndipo bwino lake uyankhe mafunso onse otsatira.

Pa mudzi wa Jeremiya womwe unali woyandikana ndi mudzi wa Zembeni munali atsikana akumaso kwa anthu. Ena mwa iwo anali Malita, Maligerita, Zelipa ndi Zaliwe. Atsikanawa anali cikoka ca anyamata m'mudzi muja. Motero, anyamata ambiri anayesera umu ndi umu kufunsira atsikanawo koma anakanidwa.

www.eczpastpapers.com

Atsikana akumaso kwa anthuwa nthawi zina anali kupita ku mudzi wa Kaunje kukaonererako magule osiyana-siyana monga cimtali citere kadayi ndi gule wa mkulu. Kumaguleko anali kukumana ndi atsikana ocokera ku mudzi wa Kaunje. Atsikanawo a kwa Lubeya anali kucitira kaduka atsikana aja a kwa Jeremiya cifukwa ca maonekedwe ao. Amakhumbiridwa, cifukwa amuna samacoka pa msana pao kusiyana ndi iwo amene amacita kulakalaka amuna oti ndi kuwapatsako cabe moni.

Tsiku lina pamudzipo pa Jeremiya panadza anyamata anai kucokera ku mzinda waukulu wa Lusaka. Maina ya anyamatawo yanali Timoti, Luka, Manyoni ndi Yohane. Iwowa anadza kudzacita nchito za malonda.

Zaliwe ataona anyamatawo anafunitsitsa kuti mwina ndi kukokako mtima m'modzi mwa iwo kuti amufunsire. Izi zinali tero cifukwa iye anali namwali wotopa.

Monga mwa khumbo lake, m'modzi mwa anyamatawo, Manyoni wabvidzo, anakodwa mu msampha nafunsira mtsikanayo. Bwino lake anamanga banja. Banjalo linali losiririka. Mkupita kwa nthawi Zaliwe anayedzeka ana anai ndi Luka. Maina ya anawo yanali Jairo, Jeriko, Kaude ndi Mphatso. Mphatso anali mwana wamkazi yekhayo. Koma mwatsoka lanji anabadwa mzungu dala. Cifukwa ca mabadwidwe amwanayo anakanidwa ndi atate ake motero, bamboyo anathetsa ukwati uja ndi kupita ku kakwatira ku mudzi wina wochedwa Kaunje.

Mbiri yakuti Zaliwe analekedwa, inafala m'midzi yonse yozungulira. Ndiye oyamwa lina maka-maka atsikana aja a kwa Kadzipalire anakondwera kwambiri cifukwa ca nkhaniyi. Nyanyiwe ndiye amene anakondwera koposa ndipo anali kulankhulira Zaliwe mau akhambi.

Mauwa yanakhalitsa Zaliwe yempha-yempha motero kuti analibe cocita cina ciri conse koma kungocirandira ndi kupitiriza ndi umoyo wake.

Atazilandira concu, anaganizira zophunzitsa ana ake aja. Indedi anao anaphunzira koma mobvutikira cifukwa ca kusowera kwa mai wawoyo. Koma cokwinyiritsa Zaliwe cinali cakuti iye anali kubvutikira ana ake aja pamene bambo wao uja anali moyo ndinso shasha. Zonsezi anagoziyikiza m'manja ya Chauta.

Mwa phamvu ya Nyamalenga, ana aja onse anai anamaliza maphunziro ao. Bwino lake analowa nchito za m'boma. Jairo anakhala mphunzi pamene Jeriko ndi Kande analowa nchito ya ugalakaca. Posimba za Mphatso, iye anakhala dotolo wa m'cipatala.

Anawo pofuna kuwongola kholo lao msana anawamangira nyumba ya bwino yamakono, ndi kuwaguliranso galimoto la makononso.

Mbiri ya kukhupuka kwa Zaliwe inafalanso m'midzi yoyandikanayo. Bwino lake mbiriyi inamufikiranso Manyoni. Koma idamuphweteka mumtima. Analaka-laka kubwererana ndi mkazi wake uja koma anadzitsutsa yekha poganizira za nkhanza zimene anamucitira. Momga amvula zakale adanenera kuti, 'Cuma cili monga m'cira wa khoswe,' bamboyo cuma cinanthawa ndipo anakhala kwakwatuke. Cifukwa ca ici anayamba kudwala matenda yothamanga mwazi (BP).

Tsiku lina zinafika pobvuta koteru kuti mosadziwa anatengedwera ku cipatala ca cikulu ca phendulo m'boma la Mkunthiwa. Ndikucipatalako, kumene anakumana ndi mwana amene anamukana.

Mwanayo mosadziwa anapereka thandizo lokwanira kwa bamboyo. Atayetsemula, anangoona kuti ali kupatsidwa mankhwala ndi mwanawakeyo.

Ici cinaliritsa bamboyo. Modabwa mphatso anafunsa cimene bamboyo anali kulira. Pomuyankha anauzidwa kuti amenewo anali atate ake. Pokumbukira zimene zinacitikira amai ake aja cifukwa ca iye anayambanso kulira.

Apa ukulemba mayeso yakoyo, anthuwa akali ciririre m'cipatala cija.

Tsopano yankhani mafunso otsatirawa.

- 1 Kodi mau akuti, 'akumanso kwa anthu' yatanthaunzanji? [2]
 - A Anthu okonda kuona kumaso
 - B Anthu okondedwa kwambiri
 - C Kudukidwa kwa anthu
 - D Kukongola kodabwitsa anthu
- 2 Ndi m'mudzi uti m'mene mumabvinidwa magule osiyana-siyana? [2]
 - A Jeremiya
 - B Kadzipalire
 - C Kaunje
 - D Zembeni

- 3 ... ndiye anakwatira Zaliwe. [2]
A Luka
B Manyoni
C Timoti
D Yohane
- 4 Kodi anyamata amene anabwera m'mudzi wa Jeremiya anadzakatani? Kudza ... [2]
A cita za Malonda.
B funsira Mbete.
C manga nyumba.
D yendera abale.
- 5 Kodi liu lakuti 'khumbo' lithanthauzanji? [2]
A Cifuniro
B Ciyembekezo
C Cizolowezi
D Kusirira
- 6 Chula dzina la mwana wa mkazi wa Zaliwe. [2]
A Maligelita
B Malita
C Mphatso
D Nyanyiwe
- 7 N'cifukwa ciyani atsikana a kwa Kaunje amacitira kaduka atsikana a kwa Jeremiya? [2]
 Anali ...
A abvidzo.
B okongola.
C ophunzira.
D onyoza.
- 8 Pereka liu fanane la liu lakuti, 'shasha'. Ndi munthu wa ... [2]
A cuma.
B manyazi.
C nthanthi.
D ulesi.
- 9 Kodi ndi phunziro lanji limene utengamo m'nkhani wawerengayi? [2]
A Kuchuka kulibe phindu
B Kuthetsa cikwati ndi kulanga munthu
C Malonda abweretsa mabvuto
D Maphunziro ndi aphindu
- 10 Nanga mutu woyenera wa nkhanayi n'kukhala uti? [2]
A Kukongola kutukwanitsa
B Kulimbikira kwa Zaliwe
C Menyani athawa mkazi
D Mphatso athetsa cikwati

Tsopano yankhani mafunso otsatirawa polemba ziganizo zathunthu ndiponso zobvomerezeka.

- 11 Kodi ndi ciyani cinathetsa ukwati wa Zaliwe ndi Manyoni? [2]
- 12 Ndi ciyani cinakondweretsa kopasa Nyanyiwe? [2]
- 13 Kodi mau abole ndi mau otani? [2]
- 14 Ndi ciyani cinabvuta Zaliwe mumtima? [2]
- 15 Nanga Mphatso anakumana bwanji ndi atate ake? [2]

D CIGAWO CACINAI – CIFUPIKITSO: [MAKISI: 20]

Werenga mosamala nkhanu yotsatira iri munsimu. Bwino lake ulembe nsonga zisanu ndi zittu zolunjika pa koipa kodula mitengo ciduledule.

Mitengo

Pa dziko lino la pansi tiona kuti cilengedwe ciri conse ciri ndi phindu lake. Pa cifukwa ici tidzaona pa cilengedwe ca mitengo.

Mitengo iri pa mitundu yosiyana-siyana, imene igwiritsidwa nchito mosiyana-siyananso.

Ena amasimba kuti ku mitengo amapatako matabwa. Matabwayo amapangirako zinthu zosiyana-siyana monga magome, mipando ndi zitseko kuchulapo zocepa cabe. Zoterezi zimadzetsa gwero la cipululu mdera. Cipululu cikapangika tero mphepo imawomba ndi kuwuluzana nthaka. Mwinaso madzi yoyenda mothamanga yamakokolola nthaka.

Anthu ena amasimbanso kuti mitengo imawapatsa nkhanu. Indedi nkhanu ndi zofunikira pa umoyo wa munthu koma ngati mitengo yadulidwa mosasamalira imatha. Kotero kuti mphepo ikamawomba, imabvumbula madenga a nyumba za anthu ndi zomanga manga zina.

Gulu lina la anthu limanena kuti mitengo imadulidwa ndi kutenthedwa ndi colinga cofuna kugwiritsira nchito pulusa ngati mfunda. Koma pofuna kupanga mfunda wokwanira mitengo yambiri-mbirinso imayenera kudulidwanso. Motero, nyengo imasokonezeka. Mvula siyimagwa pa nthawi yake mwinanso kumatentha mopitirira muyeso.

Umboni wina uliponso wakuti mitengo imagwiritsidwira nchito pazomanga-manga monga nsici, phaso ndi bwalidzo kuchulako pang'ono cabe. Mkupita kwa nthawi, mitengo imapita niyitha pang'ono-pang'ono. Zikatero tiona kuti mpheya wofunikira kupumidwa ndi anthu ukhala wosayenera. Cifukwa mitengo yoyeretsa mpheya woyipayo yanadulidwa.

Mopitirizapo, akulu-akulu atha kunena kuti m'mitengo mumagwa zidoyo zosiyana-siyana monga nthowa, mapala zinkhuwala ndi zithole kungo chulako zocepa cabe. Zidoyozo zimakhala ndiwo zokometsera kwambiri. Pofuna kupatako ndiwo kapena makhobiri, mitengo yambiri-mbiri imadulidwa ndi lingo lofuna kugwira zidoyozo zokwanira congo tiona kuti mitengo imadulidwa momvetsa cisoni. Zitatero tiona kuti

nyama za mthengo ziyamba kuthawira kutali kumene kuli thengo cifukwa cosowa pobisala.

Mowonjezerapo, mitengo imadulidwa ndi lingo lofuna kupatako cuma. Mitengo ya mtengo wapatali monga mukula uli paciopsyezo ca cikulu. Cifukwa ca ici m'malo mupezeka mitengo yotereyi imadulidwa cidulidwe-dulidwe. Yatadulidwa conco, tiona kuti zomera ku mitengo monga bowa, kanjeza ndi zina zotero zisowa cifukwa mitengo inadulidwa.

Pothera, titha kunena kuti mitengo imadulidwa cifukwa cakubalana kwa anthu. Anthu atabalana conco, amafuna polima. Ndi khumbo lofuna kupata zambiri, malo yayakulu yamadulidwa mitengo. Ndiye zikakhala conco nthaka iyamba kuguga cifukwa mitengo imene imayoyola mayani yomwe yatawolera yamakhala mfunda yanadulidwa. Pa zifukwa izi, tiyeni tisamalire mitengo ku madera komwe tikhala, ndi colinga cofuna kuteteza zomera ndi nthaka.

Mayeso Ako Atha!

www.eczpastpapers.com